



UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO
NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO
NYENGO MSABATAYI
KUYAMBIRA PA 27 JANUARY MPAKA PA 02 FEBRUARY 2025


NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Sabatayi tiyembekezere nyengo ya mvula m'madera ambiri yomwe idzigwa wamphamvu nthawi zina kamba ka dera la m'pweya opepuka lomwe liri pakati pa dziko la Madagascar ndi Mozambique. **Mvulayi ili ndi kuthekela kubweretsa mavuto akusefukira kwa madzi mwadzidzi (flash floods) makamaka madera omwe ali otsika komanso mmadera omwe madzi amasefukira nthawi zambiri.**

Nthambi yoona Zanyengo ndi Kusintha kwa Nyengo (DCCMS), ipitilira kuunika ndi kulondoloza bwino za dera la m'mpweya lopepukali lomwe lili nkuthekera kufika pa Namondwe.

NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali kwa nyengo ya mvula m'madera ambiri yomwe idagwa yamphamvu makamaka m'madera am'chigawo cha kumwera, monga tikuonera mu mapu ali m'musimu omwe akuonetsa ena mwa madera omwe analandira mvula m'sabata yangothayi.



Mapu: akusonyeza kagwedwe ka mvula kuyambira pa 20 January mpaka pa 26 January, 2025

MALANGIZO M'SABATALI

- **Madzi osefukira mwadzidzidzi (flash floods):** Tikhale tcheru ndipo tipewe kuoloka madzi osefukira kapena othamanga kuti titeteze miyoyo yathu
- **Mvula ya Mabingu:** Kukamagwa mvula ya mabingu tikuyenera kubisala pamalo otetezeka bwino ndipo tipewe kubisala pansi pa mitengo.
- **Chinyezi:** Tikhale osamala ndi **nyumba kapena zimbuzi** zomwe zanyowa kwambiri ndi mvula chifukwa zitha kugwa nthawi ina ilyonse.
- **Kutelera kwa mseu ndi khungu:** Tipewe kuyendetsa galimoto mothamanga kwambiri pamseu ndi kupililiza kutsatira mwachidwi mauthenga onse a zanyengo pamene mvula ikupitilira kugwa.

Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:

The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email:

metdept@metmalawi.gov.mw, Website: www.metmalawi.gov.mw

Malo osindikizira: Blantyre

Yatulutsidwa Lamulungu pa 26 January, 2025